INTERNATIONAL BACCALAUREATE
BACCALAURÉAT INTERNATIONAL
BACHILLERATO INTERNACIONAL



**CHICHEWA A1 – STANDARD LEVEL – PAPER 1**
**CHICHEWA A1 – NIVEAU MOYEN – ÉPREUVE 1**
**CHICHEWA A1 – NIVEL MEDIO – PRUEBA 1**

Monday 8 May 2000 (morning)
Lundi 8 mai 2000 (matin)
Lunes 8 de mayo del 2000 (mañana)

3 hours / 3 heures / 3 horas

---

INSTRUCTIONS TO CANDIDATES

- Do not open this examination paper until instructed to do so.
- Section A: Write a commentary on one passage. Include in your commentary answers to all the questions set.
- Section B: Answer one essay question. Refer mainly to works studied in Part 3 (Groups of Works); references to other works are permissible but must not form the main body of your answer.

INSTRUCTIONS DESTINÉES AUX CANDIDATS

- Ne pas ouvrir cette épreuve avant d'y être autorisé.
- Section A : Écrire un commentaire sur un passage. Votre commentaire doit traiter toutes les questions posées.
- Section B : Traiter un sujet de composition. Se référer principalement aux œuvres étudiées dans la troisième partie (Groupes d'œuvres) ; les références à d'autres œuvres sont permises mais ne doivent pas constituer l'essentiel de la réponse.

INSTRUCCIONES PARA LOS ALUMNOS

- No abra esta prueba hasta que se lo autoricen.
- Sección A: Escriba un comentario sobre uno de los fragmentos. Debe incluir en su comentario respuestas a todas las preguntas de orientación.
- Sección B: Elija un tema de redacción. Su respuesta debe centrarse principalmente en las obras estudiadas para la Parte 3 (Grupos de obras); se permiten referencias a otras obras siempre que no formen la parte principal de la respuesta.

## GAWO A

*Lembani ndemanga pa funso LIMODZI lokha, 1 (a)* ***kapena*** *1 (b).*

**1.** (a)

*Werengani nkhani ili m'munsiyi ndipo mulembe ndemanga poyankha mafunso oyitsatilawo.*

Anthu onse a m'dera la Kasiyandevu anasungulumwa kwambiri kaamba ka imfa ya Mfumu Mkomakachoka. Panalibe munthu ndi mmodzi yemwe amene amamvetsa mmene mfumuyu anamwalilira poti sanadwale konse. Patsiku lometa maliro a Mfumu Mkomakachoka, Perekanani anasonkhanitsa akuluakulu anzake onse a m'mudzimo kuti asankhe munthu wodzavala dzina la Mkomakachoka. Perekanani anati, "Monga tonse tikudziwa, chautayu watigwera mwadzidzidzi zedi. Mnzathuyu watisiyira katundu wolemera amene tsopano tiyenera kuti tithandizane kumusenza. Tonsefe tikudziwa kuti m'dera lonse lino la Kasiyandevu mulibe munthu wanzeru zakuya ngati zimene anali nazo malemuyu. Uno unali mudzi wopanda mapokoso, woti mlendo aliyense akangofika, amangodziwiratu yekha kuti wafikadi pamudzi. Koma poti akuti wokoma sakhalitsa, taonani tsopano mnzathu uja watisiya, basi sitidzamuonanso. Chachikulu tsopano ndi choti ife amasiye tisungane bwinobwino kuti mzimu wa malemuyu ungatipotole makosi. Tsono poti mnyumba yopanda mzati siyikhala, pafunika munthu woti atisungire mbumbazi m'mudzi muno."
"Koma ine ndaganiza kuti tisanakambirane za munthu wodzavala dzina la Mkomakachoka, tiyambe tafufuza bwinobwino kuti tidziwe mmene malemuyu watisiyira. Imfa yotereyi siioneka chiwonekewoneke ayi. Munthu woti analibe mangawa ndi munthu wina aliyense sangafe ndi chipumphu motere. Uguwiti woterewu sunachitikepo nkale lonse m'dera lino la Kasiyandevu," anatero Lekanani.

Perekanani anati, "Ndi zoona kuti mnzathuyu wafa kankhumu, moti tonsefe takhumudwa nayo imfa yakeyi. Komatu madzi akatayika sawoleka; uyu wapita watha. Pamene pagona njovu sipalephera nkhambakamwa. Tikati tizikamba za imfa ya wotisiyayu, tilowa nazo kutchire. Kaya, alipo angatitsimikizire kuti ena analowerapo pa imfa ya nyakwawayu?"
Lekanani anati, "Komatu tikamangoyankhula mokuluwika, ndiye kuti pamudzi pano tikutha. Zinthuzitu zayamba n'kale; Kanthunkako anatisiya mwanjira yokhayokhayi. Ine ndikhulupilira kuti pamenepa pali kanthu basi."
Chenjerani anagwapo nati, "Kunena kwa ndithendithe, nanthambwe anadzitengera: pamudzi pakagwa chauta, tisamachulutse zonena ayi. Zoterezi zimafunika kuziganizira bwinobwino kukumbukira chamawa. Nkhani zoterezi ndizo zija zimapasula midzi yambiri. Nthawi zina anthufe timakonda kuthwanula maso anthuwa nkumayang'ana kutali, tayiwala kuti mwina chitsa chimakhala m'khundumu. Mau aakulu ndi amene akunena Perekanani kuti tsopano mmene mnzathuyu watisiya, tithandizane kusenza katundu amene iyeyu watisiyira. Wakufayu wasiya aphwake awiri: pamodzi ndi mlongo wao mmodzi. Pa aphwake awiriwa tiyenera kugwirapo mmodzi kuti alowe ufumu wa atsibweni wakewu."

“Mwini dzinali ndi Msandipemphe basi, palibenso wina ayi,” anatero Perekanani. “Iyeyu anachoka kalekale ndipo wakulira ku ulendo. Pakatipa timamva kuti anali ku Kawerawera; koma tsopano kumene akukhala kwenikweni sikudziwika. Tayesa kusakasaka ku malo osiyanasiyana, koma ndi iyeyu samveka mbiri ata m’pang’onong’ono. Mwa ichi, ine ndimaganiza kuti tibamusakasaka iyeyu kuti abwere adzatisungire mbumbazi m’mudzi muno.

“Msandipemphe anatchona ku Kawerawera kalekale oti sitingayembekeze iyeyu kuti ndiye adzatisungire mbumbazi pamudzi pano,” anatero Lekanani. Kenaka anapitiriza nati, “Ndiponso angakhale tinamutumizira uthenga womudziwitsa za chisonichi, pasiwapo sanaonekerepo ayi. Tikati tizidikira Msandipemphe, ndiye kuti anthu athuwa tiataya padzuwa. Kawirikawiri matchona sakumbukira zobwerera kumudzi kwao ayi. Akuluakulu m’mudzi muno ndi ambiri, ndi kwabwino kuti ife tigwirepo mmodzi wa amenewa kuti abatisungira ana m’mudzi muno za uyo wa ku ulendo kwakeko, tiziziona m’mbuyo muno. Koma munthu weniweni angatisungire mudzi uno ndi Kwadzayani basi.”

“Amenewo ndiwo mawu,” anatero Perekanani napitiriza n’kumati, “Msandipemphe sitimpeza msanga ayi. Ndiponso sitidziwa ngati iyeyu akuganiza zobwerera m’mbuyo mmene atsibweni akewa alowa m’manda.”

Akuluakulu atavomerezana kuti Kwadzayani ndiye abagwirizira ufumu wa Mkomakachoka, anatuma Perekanani ndi Lekanani kuti akamfotokozere Kwadzayani zimene iwowa anamvana. Perekanani ndi Lekanani analawira m’mawa kupita ku nyumba kwa Kwadzayani kukatula mauwa. Pamene akuluakulu awiriwa amafika pakhomo pa Kwadzayani, anapeza mwini khomoyo asanatsekule moti amachita kumutsekulitsa.

Alex T. M. Kalindawalo *M’thengo Mudalaka Njoka* (1974)

– Fotokozani mfundo zenizeni zomwe nkhaniyi yakamba.

– Fotokozani ntchito yeniyeni ya Chenjerani mu nkhaniyi.

– Lembani za momwe mlembi wa nkhaniyi wagwiritsira ntchito chiyankhulo cha Chichewa ndipo chiyankhulocho chikukometsa nkhaniyi motani?

– Kodi ndondomeko ndi dongosolo la ziganizo ndi ndime zikugwira ntchito motani mu nkhaniyi? Fotokozani.

**1.** (b)

*Werengani ndakatulo ili m'munsiyi ndipo mulembe ndemanga poyankha mafunso oyitsatilawo.*

**WAWAIKA KUTI VIPYA?**

Mbiri yachisoni yamveka
Kuti anthu ena afa.
Tingathe kufunsa yani
Amene angathe kunena,
Wawaika kuti Vipya?

Mwatani Vipya ndi inu Nyanja
Kutithera anthu athu?
"Mphepo yandivuta ine,
Kupilira ndi anthu anuwo,
An'tayikira pa Nyanja."

Funsani Vipya nd Nyanja yemwe
Anene bwino za iwo.
Anyamata okongola
Sitidziwaonanso konse.
Wawaika kuti Vipya?

Uzani Nyanja aulule
Anthu aja onse
Komwe Vipya wawaika,
Tipereka mphotho iliyonse
Kuwaombola iwo.

Mboni zanga zonse ziripo,
Sin'kadawataya konse.
Funsani anthu a ku Livingstonia,
Kaputeni wanga adziwa.

D.R. Katengeza in Chadza, E.J. *Ntchito ya Pakamwa* (1967)

– Kodi luso la kalebedwe ka ziganizo, nthetenya pa ndondomeko ya mawu ndi mamvekedwe ake, ndi ndondomeko ya ndime zikugwira ntchito yotani mu ndakatuloyi?

– Vipya ndi chinthu chopanda moyo koma m'dakatuli wayipatsa moyo chifukwa chiyani?

– Kodi m'dakatuli wapereka chithunzithunzi chotani cha sitima yotchedwa Vipya?

– Kodi ndime yotsirizayo m'ndakatuloyi ikugwira ntchito yotani ku luso la kalembedwe ka ndakatulo? M'dakatuli achisiya osalemba ndime imeneyi, kodi ndakatuloyi idakamveka bwanji?

– M'dakatuli akuonetsa bwanji kuti ngozi ya Vipya yamukhudza kwambiri?

**GAWO B**

*Yankhani funso LIMODZI lokha mwa mafunso otsatirawa. Onetsetsani kuti muyankho lanu muli mfundo za m'mabuku okwanira awiri a m'Gulu 3 omwe munawerenga.*

**2.** Fotokozani ntchito ya chilakolako cha makedzana kapena maloto a zam'tsogolo m'mabuku omwe munawerenga.

**3.** Fananitsani ndiponso siyanitsani ntchito za anthu amakhalidwe oipa m'mabuku omwe munawerenga. Kodi anthuwo ngofunika bwanji munkhaniyo? Nanga akuthandiza bwanji kuti nkhani ikule ndikupita patsogolo, **kapena** kufotokoza zolinga za mlembi wankhaniyo?

**4.** Kodi kusemphana maganizo kapena chikhalidwe ndi chikhulupiliro kukugwira ntchito yotani mumabuku omwe munawerenga? Longosolani.

**5.** Alembi ena amadziona ngati "aphunzitsi" ndipo zolemba zawo ngati "zophunzitsa" anthu. Kodi mabuku omwe munawerenga ndi opereka maphunziro? Tsimikizani.

**6.** Fananitsani ndiponso siyanitsani luso la alembi pofokotoza komwe nkhani ikuchitika ndiponso momwe ikuchitikira m'mabuku awiri omwe munawerenga.